

NJIRA YODALILIKA YOPHERA TIZILOMBO TOIPA M'MADZI OKUMWA POGWIRITSA NTCHITO KUWALA KWA DZUWA


Madzi okuda ayenera kusefedwa kaye kuti njira yogwiritsa ntchito kuwala kwa dzuwa igwire ntchito bwino. Onani ndondomeko zotsatirazi za njira yodalirika yophera tizilombo toipa m'madzi okumwa.



1 Gwiritsani ntchito mabotolo otsuka bwino a pulasitiki. Matulani mapepala ali onse amene amatidwa pa botolopo kuti muzitha kuona bwinobwino za mkati mwa botolomo. Thirani madzi osefa bwinobwino ndi kutseka botololo ndi chotsekera.



2 Ikani mabotolo anu pa dzuwa kwa maola osachepera asanu ndi limodzi (6 hours). Ngati kuli mitambo, ikani mabotolowa padzuwa kwa masiku awiri.



3 Madzi anu ndi abwino tsopano. Mukhoza kumwa kuchokera m'botolo lanu kapena pogwiritsa ntchito kapu yotsuka bwino.



4 Sungani madzi anu m'mabotolo. Gwiritsani ntchito mabotolo amene munaika padzuwa aja.



www.waterwellsforafrica.org

For more information on the SODIS method, please go to www.sodis.ch

NJIRA YODALIRIKA YOPHERA TIZILOMBO TOIPA M'MADZI OKUMWA POGWIRITSA NTCHITO KOLORINI

Pothira madontho awiri mu botolo la madzi la 1 litre kapena madontho 8 muchigubu cha madzi cha 5 litres mumapha tizilombo toipa tambiri m'madzi akumwa.



1 Gwiritsani ntchito kolorini oyenera yemwe anavomerezeka kuti mukhoza kugwiritsa ntchito mu madzi okumwa.




2 Thirani madontho awiri mu botolo la madzi la 1 litre (kapena madontho 8 mu chigubu cha madzi cha 5 litres). Ngati madzi anu sioyera kwambiri, gwiritsani ntchito madontho 4 mu botolo la madzi la 1 litre (kapena madontho 16 mu chigubu cha madzi cha 5 litres).



3 Tsekani botolo lanu ndi chotsekera ndi kukhut-chumula bwino.



4 Dikirani phindi 30 musanamwe, kuti kolorini ayambe wapha kaye tizilombo toipa topezeka m'madzi okumwa.



5 Madzi anu ndi abwino tsopano. Mukhoza kumwa kuchokera m'botolo lanu kapena pogwiritsa ntchito kapu yotsuka bwino.



[waterwellsforafrica.org](http://www.waterwellsforafrica.org)

For more information on the chlorine disinfection method, please go to: www.cdc.gov/healthywater/emergency/safe_water/personal.html